

Kutsirika munda kuti akuba asakubere zomwe walima.

Date: Tuesday, Muharram 5, 1447 2:29 PM

Views: 388

Category: Shirk > Shirk Yaikulu > Kutsirika

Question

Kutsirika munda kuti akuba asakubere zomwe walima.

Answer

Kutamandidwa konse ndi kwa Allāh!

Choyambirira: ufiti, maula komanso matsenga pa chisilamu ndi kufr (kukanira). Aliyense amene wapita kwa asing’anga kukaombedza, kukachitako maula, kufuna mankhwala a banja, a mwayi, a malonda, otsirikira munda ndi zina zotero ameneyo wakanira mu zomwe Allāh adavumbulutsa kwa Mtumiki Wake ﷻ .

Abū Hurayrah adafotokoza kuti Mtumiki wa Allāh ﷻ adati:[1]

يَلْعَلَّ زُنْ أَمَبَرَ رَفَكَ دَقَفُ، لُوقِي أَمَبُ هَقَّصَفَ، أَفَارَعُ وَأُ، أَنَهَاكَ يَتَأْنَمُ

“Aliyense amene wapita kwa sing’anga kapena bimbi; ndipo wakhulupirira mu zimene wauzidwa (kapena kupatsidwa) kumeneko, ameneyo wakanira mu zomwe zidavumbulutsidwa kwa Muhammad (ﷺ).”

Choncho, sizili zoyenera kupita kwa asing’anga kukatengako mankhwala kapena thandizo lililonse.

Chachiwiri: inu ngati msilamu yedzamirani mwa Allāh, mukhale ndi taqwā mwa Iyeyo komanso mudzipempha chikhululuko pa machimo amene mumachita. Allāh walonjeza aliyense wa taqwā kuti adzamufewetsera ma Rizq poyankhula kuti:[2]

يَلْعَلَّ لَوْكَ وَتَي نَمَوْ ﷻ بِسَتْحَيِ الْ تُتَيِّحُ نَمُ هَقُّ زَرَيَو - أَجَحَمُ ﷻ لَعَجَّيَ لَل ﷻ قَّتَي نَمَوْ ﷻ أَرْدَقِي شَلُّ لَل ﷻ لَعَجُ دَقُ ﷻ وَرَمَ أَلْبَ لَل ﷻ نِ ﷻ ﷻ هُبَسَحَ وَهَفَ لَل ﷻ

Ndipo aliyense amene angakhale ndi taqwā mwa Allāh – Iye adzamupatsa njira yotulukira (masautso amene akudutsawo) – Ndipo adzamupatsa ma Rizq kuchokera ku m’mbali zimene samaziyembekezera. Ndipo amene wayedzamira mwa Allāh – basi

ameneyo ali womukwanira (ku chilichonse). Ndithudi, Allāh adzakwaniritsa cholinga Chake. Ndithudi, Allāh adakhazikitsa pa chilichonse muyezo.

Tilibe chikhulupiriro china chopambana kuposa kudalira mwa Allāh kuti atiteteze ku zonse zomwe zili zoipa. Popeza lyeyo ndi Wakutha kutichotsera mavuto onse ngati m'mene akuyankhulira:[3]

لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَهُوَ الْغَلِيُّ لَا يَأْتِي الْفِتْنَةَ وَلَهُ السُّلْطَانُ عَلَى كُلِّ شَيْءٍ وَالْإِلَٰهُ الْوَاحِدُ الْقَهَّارُ
لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَهُوَ الْغَلِيُّ لَا يَأْتِي الْفِتْنَةَ وَلَهُ السُّلْطَانُ عَلَى كُلِّ شَيْءٍ وَالْإِلَٰهُ الْوَاحِدُ الْقَهَّارُ

Ndipo ngati Allāh wakupatsa mavuto, palibe amene angakuchotsere kupatulapo lyeyo. Ndipo ngati Iye wakupatsa ubwino – basi Iye pa zonse (zomuyenera lyeyo) ali Wakutha.

Allāh ndiye Mwini kuzindikira.

[1] Musnad Ahmad, #9536

[2] Sūrah At-Twalāq 65:2-3

[3] Sūrah Al-An'ām 6:17